

Kodi zolinga za FISPs ndi chani?

Ndondomeko ya zipangizo zaulimi zotsika mtengo (FISPs) imafuna kuchepetsa ndalama zolowa paulimi kwa alimi ang'onoang'ono kapena alimi amene amalima kuti apeze chakudya basi. Cholinga cha FISPs, monga mwa ndondomeko zoyendetsela boma, ndi:

- kuchulukitsa cholowa cha anthu osauka;
- kutsitsa mtengo wa chakudya;
- kuwonjezela kukhala ndi chakudya chokwanira;
- kupititsa patsogolo kugwiritsa ntchito zipangizo a mu ntchito ya Green Revolution;
- kuwonjezera moyo wabwino wa tsiku ndi tsiku wa alimi;
- kuwonjezera chonde mu nthaka; komanso
- kupeleka phindu la za chuma kwa alimi.

Zipangizo zotsika mtengo zimalunjika magulu a anthu osankhika, amene amatchulidwa kuti 'opindula.'

Ngati mulimi A apeleka kwa mulimi B paketi ya mbeu, mulimi B walandira phindu – choncho mulimi B ndi wopindula.

Kawirikawiri, anthu amene amalandira phukuzi la FISP (wopindula) ndi alimi amene amalima ndi cholinga chopeza chakudya basi.

Mtengo woyendetsela ntchito ya FISP umafika pakatipati pa 100 million ndi 160 million US dollars pa chaka. Kawirikawiri, ndalama zimenezi zimachokela ku boma komanso zithandizo za chitukuko.

www.acbio.org.za info@acbio.org.za Tel +27 (0)11 486 1156

african centre for biodiversity